NIKAAH YOVOMEREZEKA

Ramadhan N.A Isa
(malawiummah.com)
Islamic Information & Da'wah

http://malawiummah.com/ndondomeko-ya-nikaah/

MAWU OYAMBA

M'dzina la Allah, Wachifundo Chambiri, Wachisoni Chosatha

الحمد لله نحمده، ونستعينه، ونستغفره، ونعوذ بالله من شرور أنفسنا، ومن سيئات أعمالنا، من يهده الله فلا مضل له، ومن يضلل فلا هادي له، وأشهد أن لا إله إلا الله وحده لا شريك له، وأشهد أن محمداً عبده ورسوله، صلى الله عليه وعلى آله وأصحابه وسلم، ومن تبعهم بإحسان إلى يوم الدين

Kuyamikidwa konse ndi kwa Allah yemwe timamuyamika nthawi zonse, timapempha chithandizo chake komanso chikhululuko, ndipo timadzitchinjiriza kwa Iye kuchokera ku zoipa zammitima mwathu, ndikuzoipa zochokera muntchito zathu. Yemwe Allah wamuwongola palibe yemwe angamusocheretse, ndipo yemwe Allah wamufuna kuti asochere palibe yemwe angamuwongole. Ndikuikira umboni kuti palibe mulungu opembedzedwa muchoonadi kupatula Allah Mmodzi yekha; Iye alibe ophatikizana naye. Ndikuikiranso umboni kuti Muhammad salla Allah alaih wasallam ndi kapolo wake ndi Mtumiki wake. Allah ampatse zabwino pamodzi ndi akunyumba kwake, ma Swahaba ake komanso omwe akuwatsatira pantchito zabwino kufikira tsiku la Chiweruzo.

Uthenga womwe uli m'kabuku aka ndi waufupi kwambiri ndipo ukulongosola zinthu zikuluzikulu zomwe zili zofunikira kwambiri pa nikaah. Zinthu zimenezi ndindondomeko yokhayo yomwe ili yovomerezeka m'Chisilamu kuti mwambo wonse wa chikwati uyende mopanda kugwera ku za haram, zomwe nikaah singatheke popanda izo. Ndipo zikangotheka kutsatira zoterozo ndiye kuti palibenso mulandu uliwonse pamaso pa Allah kumbali ya nikaah. Zina zonse zomwe zimadza pambuyo pazimenezi kapena patsogolo pake, sizingalepheretse nikaah zitapanda kuchitika.

Malinga ndi kupindidwa kwa choonadi masiku ano, zikupezeka kuti anthu asiya njira yeniyeni ya nikaah yomwe Mtumiki salla Allah alaih wasallam anatisiyira, ndipo atenga njira yongodzipangira, yomwe ambiri samakwanitsa kuchita nikaah, ndipo kukwatira kwa Shariah masiku ano kukumaoneka ngati chipsinjo chifukwa cha nkhawa yomwe imadza kamba ka kuganizira za komwe angapeze chuma chogwiritsa ntchito pa nikaah.

Ndikukhulupilira kuti kabukuka kathandiza anthu okhawo omwe akufunafuna ndondomeko yeniyeni ya Chisilamu pazochitika zawo makamaka nikaah, ndipo omwe safuna, timpemphe Allah Ta'la kuti awawongole ndikuwapatsa kuzindikira mu Deen.

Ntchito yogwira munthu siilephera kupezeka zolakwika, kupatula zochita za Allah. Choncho ndikupempha aliyense amene angapeze zolakwika zirizonse kuti anditumizire ndi cholinga choti ndikhonze.

Ine m'bale wanu
Ramadhan N.A Isa
+265996526528

Gawo Loyamba

ZOFUNIKIRA PA NIKAAH

1. Okwatira

Pamene mwambo wa nikaah ukuchitikira malo aliwonse omwe anthu asankha (monga munsikiti, m'nyumba ngakhalenso mu office ya Sheikh), malo aliwonsewo omwe tikufuna kuchitiramo mwambo wa nikaah siziri zofunikira kuti mkazi yemwe akukwatiwa apezeke pa gulu koma mmalo mwake ayimilira waliyyu amr ولي أمر (muyang'aniri wa mkaziyo, yemwe akuyembekezera kumpereka kwa mwamuna).

2&3. Mboni ziwiri

Mboni ziwiri zikhale zochokera kuchimuna ndi kuchikazi, zomwe zingakhale zodalirika pokumbukira zonse zomwe zingachitike pa nikaah. Ngati mboni zakuchimuna ndi kuchikazi sizipezeka, ndi zovomerezeka kutenga mboni zirizonse kuchokera mwa anthu omwe ali odziwika kwa okwatiranawo, kuti achitire umboni wa ukwatiwo. Mbonizo zikhale zakutha kukumbukira bwinobwino zonse zomwe zichitike pa nikaapo.

4. Omukwatitsa mkazi (waliyyu amr ولي أمر)

Awa ndi bambo, bamboo aang'ono, kapena mchimwene, kapena munthu yemwe ali ndi udindo wa uyang'aniri pa mkaziyo.

Amenewa ndi anthu anayi omwe amapangitsa kuti nikah ichitike.

Zoyenera Kuyankhulidwa ndi waliyyu amri kwa mkwatibwi

Omukwatitsa mkazi (waliyyu amr ولي أمر) ayenera kuyankhula kamodzi kokha basi kumuwuza mwamuna (mkwati) kuti *"ndakukwatitsa mwana wanga"* (kapena mchemwali wanga) potengera ubale wake ndi mkaziyo. Angathenso kugwiritsa ntchito mau aliwonse womwe angatanthauze kupereka mkaziyo kwa mwamuna kuti akhale mkazi wake.

Mwamuna (mkwati) ayankhulenso kamodzi kokha basi kuti: *"ndavomera."*

Ndizabwino kuti poyambilira pakhale khutbah (khutbatul-haajah). Koma khutbah imeneyi siyokakamizidwa ndipo ingathe kuwerengedwa ndi wina aliyense. Atha kuwerenga yemwe akumuimira mkazi (waliyy), atha kuwerenga mkwati, kapena mmodzi mwa mboni ziwiri zija, ngakhalenso wina aliyense yemwe alipo panthawiyo. Nikaah ingatheke popanda kuwerenga khutbah.

5. Chiwongo (mahri)

Nzothekanso osapereka mahri nthawi yomweyo mmalo mwake kuzapereka mtsogolo ngati ngongole. Ikakhala ngongole, palembedwe mgwirizano wa

ngongoleyo potsatira malamulo olemberana ngongole, ndipo mboni ziwiri zija zichitire umboni pa nthawi yopereka ngongoleyo.

Amenewa ndiye ndi malamulo a nikaah yovomerezeka, ndipo ma Sheikh akupemphedwa kuphunzitsa anthu kutsatira ndondomekozi mofewa ndi mosakhwimitsa monga momwe Chisilamu chaphunzitsira.

Gawo Lachiwiri

MAFUNSIDWE A MAHR

Zomwe zimachitika masiku ano zobisa mahr nkudzaitanitsa nthawi yomwe nikaah ikuchitika, si chiphunzitso cha Chisilamu, komanso mboni ziwiri kufunsa mahr tsiku la nikaah sichiphunzitso cha Chisilamu.

Mahr imayenera kukhala ikudziwika kwa waliyy (muyang'aniri wa mkazi) pomafika tsiku la nikaah, ndipo (waliyy) ayenera kulandira mahr mmalo mwa mkaziyo ndikukamupatsa mwamuna pambuyo pa mwambo wa nikaah.

Zomapita kukafunsa mahr kwa azimayi tsiku la nikaah ndi zina mwa zomwe zili zolakwika, ndipo zobweretsa chisokonezo mu Chipembedzo, komanso ndi njira yopangitsa kusakanikirana kwa azibambo ndi azimayi, zomwe ndi uchimo ku Chipembedzo cha Allah (Chisilamu), Chipembedzo chokhacho chomwe ndi cha Allah, pomwe zipembedzo zinazi ndi zabodza ndipo zopeka, anthu ake amangodzipangira zawozawo zomwe afuna panthawiyo, zopanda ndondomeko ya umulungu wa Mlengi wawo.

Mkwatibwi asapezeke pagulu la amun a kuti alandire mahri kapena certificate. Ngati amuna ndi azimai akhala mosiyana, pasapezeke amuna ena kulowa kwa azimai ncholinga chokatenga mahr yomwe mkazi waitanitsa. Mkazi asafunsidwe kuti *"mahri zingati?"* kapena *"mahri yake ndi chani?"* kuti kenako ayankhule potchula mahr. Monga mmene tanenera kale, maitanitsidwe a mahri oterowo ndiosemphana ndi chiphunzitso cha Chisilamu.

Mwambo wa nikaah ya Chipembezo choonadi cha Allah opembezedwa mu choonadi, uyenera kukhala osiyana ndi mwambo wa ukwati wa zipembedzo zabodza ndi zopeka.

Nikaah yeniyeni ya malamulo a Chisilamu imachitika mosapitilira mphindi zisanu 5 ngati khutba itachitika, ndipo ngati khutba palibe, pa mphindi imodzi yokha nikaah imakhala yatha. Pa nikaah sipamakhala mwambo wina uliwonse kuposa kukwatitsa; kusiyana ndi walima (chikondwelero cha nikaah), ndipo ndi zofunika kusiyatsa pakati pa nikaah ndi walima.

Ma sheikh akuyenera kuphunzitsa anthu ndondomeko yofewa ya nikaah malinga ndi chiphunzitso cha Sunnah. Ndipo asalekelere mchitidwe wa nikaah woononga komanso wodzetsa mantha mmitima ya Asilamu omwe sanakwatire. Achinyamata ambiri amakhala akuopa kupanga nikaah chifukwa cha kusokonezeka ndi zochitika za mmanikaah ena, zomwe zimawaopseza kuti sangakwanitse malinga ndi kuchepekedwa kwa mthumba. Masheikh aphunzitse zoona zenizeni zoti Nikaah yolondola simafuna ndalama zoti mpaka kulepheretsa mwambo. Achite nikaah ndipo walimah adzachite tsiku lina akadzakhonzeka bwinobwino.

Gawo Lachitatu

WALIMAH

Walimah ndi phwando kapena chisangalalo chomwe chimabwera kumapeto komangitsa banja (Nikaah).

Ndizololedwa kuchita walimah nthawi yomweyo kapena kuchedwetsa malingana ndi kuthekera kwa munthu, ndipo iyenera kuchitika munjira yomwe ili yololedwa ndi malamulo a Chisilamu; zilizonse zomwe zili zoletsedwa mChisilamu monga nyimbo, kusakanikirana kwa akazi ndi amuna, kuimba ndikuvina kwa azimayi pamaso pa amuna, zonsezo ndizoletsedwa pa chisangalalo cha nikaah (walimah).

Ngati Nikaah yayenda bwino ndipo walimah yachitika mwa haraam, zimakhala nsambi za padera zomwe ndi tchimo koma nsambi zake sizimaononga nikaah. Koma ngakhale kuti tchimo la pawalimah silikuononga nikaah, sitikulimbikitsa kuchita zoipazo, chifukwa Chisilamu chikuletsa kwatunthu kupanga zirizonse za haram nthawi ina iriyoye. Ndiye sikuti titengere mwayi kuti poti walimah ya haraam simaononga nikaah.

Pomaliza tikumbutsane kuti nikaah ndi mapemphero (Ibaadah) omwe Mtumiki salla Allah alaih wasallam anachita kuwatchula kuti ndi njira (Sunnah) yake, choncho zikufunika kutsatira chiphunzitso cha Mtumiki ndikupewa zopeka zomwe zilibe umboni uliwonse komanso zomwe zikutsutsana ndi chiphunzitso cha Chisilamu pa mwambo wa nikaah. Mtumiki salla Allah alaih wasallam analimbikitsa kuchita walimah, choncho titsatire ndondomeko yake kuti tisaipitse chiphunzitso choyera cha Mtumiki.

Gawo Lachinayi

MAVALIDWE A PA NIKAAH NDI PA WALIMAH

Kusiyana kwa veil ndi wedding dress

Ma Sheikh odalirika pamaphunziro a Chisilamu akhala akuchilimika kuletsa chovala chija chotchedwa **"veil"** pa nikaah. Lero tikufuna tichitirepo chidwi ndi kufotokoza momveka bwino pa nkhani imeneyi kuti aliyense atenge choonadi cha chovala chimenechi.

Kodi veil ndo chovala cha Chikhrisitu? Kodi Asilamu ndiololedwa kuvala?

Liwu loti "Veil/ Veiling ndi liwu la English ndipo mu Chichewa likutanthawuza kuti "kuphimba/kuvinkira". Mu Arabic kutanthawuza Tahajjub/Hijaab.

Wedding dress ndi Veil

Tikuyenera kusiyanitsa pakati pa wedding dress ndi veil; veil ndi chovala cha Msilamu aliyense wamwamuna ndi wamkazi pobisa maliseche ake (hijaab). Hijaab ndi chovala chovindikira maliseche a munthu wina aliyense, ndipo kuvala kobisa maliseche kuli kokakamizidwa mbali zonse za azibambo ndi azimayi omwe, komanso malamulo ndi ma conditions a chovala chobisa maliseche ndi ofanana kwa mkazi ndi mwamuna; kuti chikhale chokhuthala komanso chosathina. Kuvala zovala zothina komanso zopyapyala zoonekera mkati ndi koletsedwa kwa mwamuna ndi mkazi yemwe.

Kusiyana kwa mavalidwe a veil ndi oti mwamuna amavindikira mbali ya thupi lake lochepa pamene mkazi amavindikira thupi lonse kupatula nkhope ndi manja ake okha basi, kapena thupi lonse nkusiya maso okha (niqaab).

Wedding dress ndi chovala chomwe mkazi kapena mwamuna amakhonza kuti adzavale pa ukwati wake.

Kutanthauza kwa *wedding dress* ndiko kuti chovala cha tsiku la ukwati/Nikah pa walimah. Munthu aliyense wamkazi kapena wamwamuna amakonzekera chovala chake chomwe adzavale pa mwambo uliwonse womwe uli wa pamwamba, ndipo chovalacho chimakhala chovala cha mwambo umenewo. Ukakhala ukwati Nikah/walimah kapena wedding, chovalacho chidzatenga dzina la mwambo wa nikah/walimah kapena wedding malingana ndi chilankhulo chomwe anthu achikonda.

Tsopano malamulo a wedding dress akhala malamulo a kuvala kwa Chisilamu, kaya mwamuna kaya mkazi; atsatire malamulo akuvala kwa Chisilamu pa chovala chake chomwe akufuna kuvala malingana ndi pa gulu pomwe akapezekepo.

Tsopano nkhani ya malamulo a kuvala kwa mtsikana yemwe akukwatiwa, ndi yosasiyana ndi mnyamata yemwe akukwatiwa.

Tisaiwale, azimayi azikhala kwa azimayi okhaokha pa walimah ndipo ngati atakhala limodzi (azibambo ndi azimayi malo amodzi), onsewo ayenera kuvala motsatira malamulo a Chisilamu ndipo azimayi ayenera kukhala chete, asalongolole komanso asadzigwedezegwedeze. Ndipo adzakhala m'mbuyo mwa azibambo, sakuyenera kuimba chirichonse kapena kukweza mawu awo. Kwawo azimayi kudzakhala kumvera zolankhula za azibambo pa mwambo uli onse omwe azimayi ndi azibambo apezekera pamodzi.

Koma ngati azibambo ali kwawo azimayinso kwawo sakuonana, onse adzakhala otakasuka pakati pawo; azimayi pakati pa azimayi avale momasukirana, chimodzimodzinso azibambo.

Choncho sitikuona cholinga chilichonse chopelekera malamulo a wedding dress kwa azimayi, chifukwa Walimah yabwino ndi yomwe azimayi akhala kwawokha azibambonso kwawokha; kuti azimayi akhale omasuka kupanga zinthu zomwe sangapange pamaso pa azibambo.

Masheikh omwe amalimbikitsa mtsikana okwatiwa kuvala modziphimba tsiku la walimah amafuna kuti mtsikana okwatiwayo azikafika kugulu la azibambo, izi sizololedwa mu Chisilamu. Azimayi azikhala kwawo azibambonso kwawo kuti onse azitha kumasuka ndi kusangalala mokwanira, chifukwa tsiku la walimah ndi tsiku la chisangalalo, si tsiku lomangana.

Veil ndi liwu la "English" kutanthawuza kuti "Chodzivindikira nacho". Veiling ndi kuvinikira.

Kuvala Chovala Choyera:

Chovala choyera ndi chokondedwa ndi Mtumiki ndipo kuvala chovala choyera ndi zabwino mu Chisilamu nthawi ina iliyonse, kuphatikizapo mma walimah. Choncho ngati timaona akhristu akuvala zoyera mmaukwatui awo, anatengera Asilamu, koma kuti iwowo amachikhonza mmakhonzedwe osemphana ndi Chisilamu. Choncho Msilamu sakuyenera kusiya kuvala zovala za white kamba koti akhristu amavala. Kukakhala kutengera, iwowo ndamene anatengera Asilamu ndipo kutengera koletsedwa ndikomwe kumachitika pamakhonzedwe a chovalacho (kuthina, kuonekera mkati ndi zina zotero). Choncho Msilamu avale zoyera koma asatyengere masokedwe a chikhristu.

Kudzivunukula Tsiku la Walimah

Pomaliza mwa chidule kwambiri, kuchotsa mpango kumutu ndikudzivunukula tsiku la walima pakati pa azimayi okhaokha ndi kumacheza ngati chikhalidwe pokondwerera kwawo, sindikupeza umboni woletsa zimenezo.

Timvetsetsane kuti **veil kapena popanda veil,** mzimayi okwatiwa ndi azimayi onse asapezeke ku chigulu cha azibambo! Ndipo kamba kakuti akhala kugulu la azimayi okha okha, mtsikana okwatiwa ali omasuka kuvala zina zili zonse pakati

pa azimayi, zosaonetsa maliseche. Komanso omwe amalimbikitsana zokonza mavalidwe amkazi okwatiwa pa Nikaah ndi walima, akungofuna azimayi azisakanikirana ndi azibambo.

Tikulangizeni kuti palibe ضرورة (kufunikira) kulikonse komwe kukupangitsa kuti azimayi ndi azibambo asakanikirane pa nikah kapena pa Walimah.

Azimai aziwuzidwa za kavalidwe popita ku mzikiti kapena kukamvera ma ulaliki a Allah ndi kunja kwina kuli konse komwe iwo afuna kupita komwe atha kukumana ndi azibambo.

Kuphunzitsa mavalidwe a mzimayi pa nikaah kapena pa walimah, kumeneko ndikutuma azimayi kuti azisakanikirana ndi azibambo, zomwe mu Chisilamu ndi zoletsedwa. Chisilamu chinaphunzitsa kale mavalidwe a mzimai malo aliwonse, ndipo palibe kuvala kwaspecial pa nikaah koposa komwe Chisilamu chinaphunzitsa. Ngati mukuphunzitsa mavalidwe a special pa nikaah, ndi zomwe mukubweretsa ma fitnazi.

Akhristu okwatirana amavulana veil pakati pa okwatira ndi okwatiwa pa chigulu cha amuna ndi akazi komanso ana, ndikuvekana ma ring komanso kupsopsonana mowakhumbidza anthu ndi kumawaombera mmanja. Zonsezo sangapange Msilamu otsatira malamulo tanena aja. Anthu oti sanasakanikirane sangapeze nthawi yovulana veil pagulu, kuvekana ring kapena kupsopsonana ngati mwambo wapadera pakati pa gulu la anthu, chifukwa ingasowe nthawi ndi malo opezerana.

Kuvulana veil, kuvekana ring, kupsopsonana komanso ku hagana kwa pagulu ndizolakwika mu Chisilamu.

Malinga ndi maganizidwe a anthu ena pa nkhaniyi, ndikufuna ndichenjeze kuti masiku athu ano bodza likakhanzikika limasanduka choonadi. Ndipo

حين سكت أهل الحق عن الباطل توهم أهل الباطل أنهم على حق

“Pamene ozindikira za Haqq (zoona, ma Sheikh, akakhala chete pamene zoipa zikuchitika), ochita zoipa amaganiza (ndipo amakhulupilira) kuti ali mu choonadi, (amaganiza kuti akulondola ndithu, ndipo akuchita malinga ndi Shariah).

Choncho ma Sheikh akuyenera kuletsa zinthu zolakwika pamene zikuchitika pakati pa Ummah, ndipo asamudandaule munthu aliyense kapena kusamala ubale wapakati pawo, koma asamale ubale wapakati pa iwon (Sheikhwo) ndi Allah Ta’la, chifukwa Iye ndiyemwe adzafinse Tsiku la Qiyamah ndikuwalipira ntchito zawozo, osati anthu.

Gawo Lachisanu

BRIDAL SHOWER MCHISILAMU

Liwu loti *"Bridal" (bride to be)* likuimira mkazi yemwe ali ndi ukwati wake posachedwa. *"Shower"* ndi kupereka mwambo ndi mphatso komanso madalitso ndi malangizo ndi kumukondwelera pamene azikakhala m'banja ndi mwamuna wake.

Malingana ndi matanthauzo awa a *"bridal shower",* zikusemphana kwambiri ndi chiphunzitso cha Chisilamu, chifukwa kupereka mphatso kapena kusangalalira mtsikana ndi kumufunira mafuno abwino pa kukwatiwa kwake ziyenera kuti zidzikhala mu gulu la chikondwelero cha nikaah (walimah). Izi zikutanthauza kuti ziyenera zizikhala kumapeto kwa nikaah osati nikaah isanachitike.

Kuchita mwambo oterewu ndi kulakwa kwakukulu mu Chipembedzo cha Chisilamu, chifukwa ndi zopeka zomwe Mtumiki salla Allah alaih wasallam sanachite pa mwambo wa nikaah. Tisaiwale kuti nikaah ndi mapemphero (ibaadah), ndipo palibe ibaada yomwe imachitika mChislamu kupatula yochokera mu Qur'an kapena mu Sunnah. Bridal Shower sikupezeka mu Qur'an kapena mu Sunnah, mundondomeko ya ukwati.

Poonjezera apo, nthawi zina nikaah imatha kulephereka osachitika *bridal shower* itachitika kale, malingana ndi kusemphana maganizo kwa anthu okwatirana komwe kumatha kuchitika nikaah isanachitike, ndikusakwatirana zonse nkukanika. Zikakanika chonchi, ndiye kuti zonse zomwe apanga pa *bridal shower* zimakhala zaonongeka – kuyambira nthawi komanso chuma – ndiponso mtsikanayo amakhala kuti wasokonezedwa nzeru zake. (Allah samakonda anthu oononga). Choncho ndibwino kupewa zinthu zomwe mu Chipembezo mulibe komanso zomwe zimachitika nthawi yosayenera.

Ndikofunikira kumusangalalira mtsikana ndi mnyamata amene wakwatira kapena wakwatiwa ndi kumufunira zabwino ponena mawu oti ***Baarakallah fiikumaa wa baaraka 'alykuma wa jama' bainakumaa bil-khair.***

Apa mungapereke malangizo osiyanasiyana komanso mutha kupereka mphatso pagulu la azimayi okhaokha, atapanga nikaah, uku mukumusangalalira ngati gawo la walimah ndipo zidzalowa mu walimah osati *bridal shower* ya bid'ahyo.

Tikumbutsane kuti Nikaah simalonda opezerapo ndalama ayi, koma ndigawo la mapemphero potsatira chiphunzitso cha Chisilamu.

Tinene momveka bwino kuti ndi zolakwika kuyenda azimayi kupita kulikonse ulendo oyenda usiku ndi usana ngakhale ulendowo uli ofunika bwanji, kupatula kuthawa nkhondo poteteza moyo wake (mkaziyo). Choncho kupita ku walima kaya ku hajj ku maulendo a mwambo wa Chisilamu kapena ku mapemphero

aliwonse, ndi zosavomerezedwa mkazi kuyenda popanda mahram wake, ngati kupita ndi kubwera ku ulendowo kukupitilira gawo lamasana. Ndipo ngati ndi zoletsedwa kutero pa mwambo wa Chisilamu kapena ku mapemphero aliwonse, ndiye kuti mzimayi atalikire kwatunthu kuyenda popanda mahram pa myambo ya chikunja ndi yosakhala mapemphero a Chisilamu yomwe ngati *bridal party* kapena *bridal shower.*

Pomaliza tikumbutsane kuti mzimayi sangakhale mahram kwa mzimayi mzake ngakhale ali chigulu, azimayiwo sakuloledwa kuyenda okha chifukwa chosowa mahram wawo. Mahram ndi m'bale wachimuna wamkazi (mlongo wake, bambo wake etc) kapena mwamuna wake.

MAWU OMALIZA

Ndikupemphera zabwino Mtumiki wa Allah, Muhammad salla Allah alaih wasallam, akubanja lake, ma Swahaba ake komanso onse omwe akuwatsatira pantchito zabwino mpaka tsiku la Chiweruzo.

Ndikupempha Allah adalitse aliyense yemwe angawerenge uthengawu (kabukuka), ndikugwiritsa ntchito komanso kuwagawira anzawo.

Zolakwika zonse zomwe zingapezeke mu uthengawu sicholinga changa, Allah Ta'la ndi Yekhayo yemwe salakwitsa. Choncho ndidziwitseni zolakwikazo pondiimbira kapena kundilembera pa number yomwe ikupezeka m'kabukuka.

Allah akudalitseni

ZAMKATIMU

Mawu Oyamba	2
Zofunika pa Nikaah	4
Mafunsidwe a Mahri	6
Walimah	7
Mavalidwe	8
Bridal Shower	11
Mawu Omaliza	13